## PHUNZIRO LA 4

1. Kodi Mulungu ali ndi mnofu, mafupa kapena magazi?
-Iyayi.

2. Kodi Mulungu amafuna chakudya kuti adye ndi madzi kuti amwe?
-Iyayi.

3. Kodi ndi chifukqwa chiyani Mulungu samafuna chakudya kuti adye ndi madzi kuti amwe?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi mzimu.

4. Kodi Mulungu ali kuti?
-Mulungu ali paliponse nthavi zonse.

5. Kodi tingapite kuti tikafuna kubisala kwa Mulungu?
-Sitingathe kubisala kwa Mulungu.

6. Kodi kuli Milungu yingati?
-Kuli Mulungu mmodzi yekha.

7. Kodi Anthu atatu amene ali Mulungu mmodzi ndi ndani?
-Mulungu Atate, Mulungu Mwana (Mpulumutsi), ndi Mulungu Mzimu Woyera.

-Pachiyambi, Mulungu analenga angelo onse.

-Pachiyambi panalibe mngelo ngakhale mmodzi amene anali ndi moyo.

-Mulungu anakakhala kuti sanavalenge angelo, ndiye kuti angelowo sanakakhala ndi moyo.

-Mulungu ndi wamkulu kwambiri kuposa angelo.
-Kodi chifukwa chiyani?

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene analipo angelo asa-nalengedwe.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene analenga angelo.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anapereka moyo kwa

angelo onse.

-Mulungu atavalenga angelo, Iye sanavapatse minofu, mafupa ngakhale magazi.

-Mulungu atavalenga angelo, Iye anavalenga ngati mizimu.

-Mulungu ndi Mzimu, ndipo angelonso ndi mizimu.
-Koma Mulungu ndi wapamwamba kwambiri kuposa angelo onse.

-Mulungu akhoza kupezeka pena pali pose mu nthavi zonse.
-Koma angelo akhoza kupezeka pa malo amodzi pa nthavi imodzi.

-Ngakhale kuti Mulungu anavalenga angelo ngati mizimu yopanda minofu, mafupa ndi magazi, nthavi zina angelowo amasintha mawonekedwe awo ndikumawoneka ngati munthu.

-Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anavalenga angelo?
-Kodi Mulungu amkafuna chithandizo china chilichonse?

-Iyayi, Mulungu samafuna chithandizo china chilichonse.

-Mphamvu ya mulungu siyitha ndipo ndi yayikulu kwambiri kuposa ya angelo onse.
-Mulungu samkafuna chithandizo china chilichonse.
-Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu analenga angelo?

-Chifukwa chakuti Mulungu anavakonda angelowo.

-Mulungu anavalenga angelo kuti adzimukonda Iye.
-Mulungu anavalenga angelo kuti adzimumvera Iye.
-Mulungu anavalenga angelo kuti adzimutumikira Iye.

-Kodi  mamuna akamanga nyumba, mwini nyumbayo amakhala ndani?
-Mamuna amene wamangayo.

-Kodi ndi chifukwa chiyani?



amene amatsutsana ndi Iye.

-Lusifala anachimwa ndipo Mulungu anamusintha dzina lake.
-Mulungu analisintha dzina lakuti Lusifala kukhala Satana.
-Dzina lakuti Lusifala limatanthawuza kuti mdani.

-Satana ndi mdani wa Mulungu.
-Satana ndi mdani wa anthu onse.

-Angelo onse amene ankamutsata Satana, anachimwanso ndipo Mulungu anawasinthanso mayina awo.
-Mulungu anawasintha mayina awowo kukhala ziwanda.

-Ziwanda ndi adani a Mulungu.
-Ziwanda ndi adani a anthu onse.

-Mulungu anamuchotsa Satana kumwamba pamodzi ndi ziwanda zake.
-Tsopano Satana ndi zawanda zake, akukhala pa dziko la pansi pano.

-Satana ndi ziwanda zake amamuda Mulungu.
-Satana ndi ziwanda zake amawada anthu onse.

-Satana ndi ziwanda zake amayesayesa kuti adziwononga ntchito ya Mulungu pa dziko la pansi pano.

-Satana ndi ziwanda zake, usana ndi usiku amalimbana ndi ntchito ya Mulungu.

-Kodi bambo akewo amene anali amphanvu ndiponso a nzeru kwambiri anakamulola mwana wawo amene anali opanda nzeru ndipo wa ulesi kuti alande ufumu wawowo?
-Iyayi.

-Kodi amene ali ndi mphanvu zambiri kuposa Mulungu ndi ndani?
-Palibe.

-Kodi amene ali ndi nzeru kwambiri kuposa Mulungu ndi ndani?
-Palibe.

-Kodi Mulungu anakamulola Lusifala kuti alande udindo wake?
-Iyayi.

-Mulungu anakwiya kwambiri ndi Lusifala ndipo anamuchotsa kumwamba.

-Mulungunso anakwiya kwambiri ndi angelo amene anamutsata Lusifala, ndipo anavachotsa onse kumwamba.

-Mulungu anakonza malo owopsya kwambiri a chilango chosatha kwa Lusifala ndi angelo onse amene anamutsata iye.

-Malova amatchedwa kuti Nyanja ya Moto Wosatha.

-Tsiku lina, Mulungu adzamutumiza Lusifala ndi angelo onse amene anamutsata iye  ku Nyanja ya Moto Wosatha.

-Mulungu ndi wabwino kwambiri ndipo sachimwa, koma amadana ndi machimo.

-Mulungu ndi wabwino kwambiri ndipo sachimwa, koma nthawi zonse amapereka chilango kwa anthu amene samumvera Iye.

-Nthawi zonse Mulungu amapereka chilango kwa anthu



-Chifukwa chakuti mamunayo ndi amene wamanga nyumbayo.

-Kodi mkazi akawumba mbiya, mwini mbiyayo amakhala ndani?
-Mkazi amene wawumba mbiyayo.

-Kodi ndi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti mkaziyo ndi amene wawumba mbiyayo.

-Kodi nanga ngati Mulungu ndi amene analenga angelo, mwini angelowo ndi ndani?
-Mulungu.

-Kodi ndi chikukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene analenga angelowo.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene analenga angelo, angelowo ndi a Mulungu.

-Kodi Mulungu analenga angelo oyipa kapena abwino?
-Mulungu analenga angelo onse abwino.
-Mulungu ndi wabwino kwambiri.
-Mulungu sangapange china chilichonse choyipa.

-Zonse zimene amaganiza Mulungu zimakhala zabwino zokhazokha.
-Zonse zimene amayankhula Mulungu zimakhala zabwino zokhazokha.
-Zonse zimene amachita Mulungu zimakhala zabwino zokhazokha.

-Mulungu ndi wabwino kwambiri.
-Mulungu sangapange china chilichonse choyipa.
-Mulungu anavalenga angelo onse abwino okhaokha.

-Mulungu analenga angelo ndi kuvapatsa mphamvu zambiri.

-Mulungu anavalenga angelo ndi kuvapatsa nzeru zambiri.

-Mulungu yekha ndi amene ali ndi mphamvu zambiri kuposa

za angelo.
-Mulungu yekha ndi amene ali ndi mzeru zambiri kuposa za angelo.

-Kodi Mulungu analenga angelo angati?
-Mulungu analenga angelo ambiri, ndipo sitingathe kuvaverenga onse.

-Pachiyambi, angelo onse amene Mulungu anavalenga anali abwino wokhawokha.
-Pachiyambi, angelo onse amene Mulungu anavalenga amakhala ndi Mulungu kumwamba.

-Kodi kumwamba ndi chiyani?
-Kumwamba ndi malo a Mulungu osafanana ndi malo ena ali onse kumene Iye amakhalako.

-Kodi kumwamba kuli kuti?
-Sitikukudziva, koma kumwamba ndi ku malo koposa kumlengalenga  kumene kuli mwezi, dzuwa, ndi nyenyezi.

-Mulungu analenga mngelo m.modzi kukhala wamkulu kuposa angelo ena onse.
-Dzina la mngelo wamkulu kwambiri kuposa angelo ena onse linali Lusifala.

-Mulungu anamupatsa Lusifala mphamvu zambiri kuposa angelo ena onse.
-Mulungu anamupatsa Lusifala mzeru zambiri kuposa angelo ena onse.

-Mulungu yekha ndi amene anali ndi mphamvu zambiri kuposa Lisifala.
-Mulungu yekha ndi amene anali ndi mzeru zambiri kuposa Lusufala.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamulenga Lusifala, kodi Lusifalayo anali wandani?
-Mulungu.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamulenga Lusifala, kodi Lusifalayo amayenera kumumvera ndani?
-Mulungu.



-Tsiku limodzi, Lusifala anaziyang'ana mphamvu zonse zimene iye anali nazo, ndipo anayamba kunyada.
-Tsiku limodzi, Lusifala anaziyang'ana mzeru zake zonse zimene iye anali nazo, ndipo anayamba kunyada.

-Lusifala anayamba kunyada, ndipo amkafuna kumulanda udindo Mulungu.
-Lusifala anayamba kunyada,  ndipo amkafuna kuti iye akhale Mulungu.
-Lusifala anayamba kunyada, ndipo anali oyamba kupanga tchimo.

-Kodi tchimo ndi chiyani?
-Tchimo ndi china chake chimene Mulungu samachifuna.
-Tchimo ndi china chilichonse chimene Mulungu samachifuna.

-Kodi Mulungu amkadziva kuti Lusifala amkafuna kumulanda udindo?
-Inde.

-Mulungu anazidziva zonse chimene Lusifala anakonza kuti azichite.

-Mulungu anavadziva maganizo onse a Lusifala.
-Mulungu anavadziva maganizo onse a Lusifala iye asanayambe kuvaganiza.

-Mulungu amavadziva maganizo athu onse.
-Mulungu amavadziva maganizo athu onse tisanayambe kuvaganiza.

-Apa pali chitsanzo:

-Munthu wina wake wamphamvu ndiponso wanzeru kwambiri anali mfumu mmudzi mwake.
-Tsiku lina lake mwana wake amene anali opanda nzeru ndiponso wa ulesi anaganiza zolanda ufumu wa bambo ake.